NAME: ______________________________(CHONGANI) DAY/OPEN



# CENTRAL EAST EDUCATION DIVISION

## 2026 MSCE MOCK EXAMINATION

# CHICHEWA

**Monday, 23 March** **Time Allowed: 1 hour 45 min**

**2:00 pm – 3:45 pm**

## PAPER I

(Malikisi 60)

**Malangizo**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi atatu.**

2. **Pepalali lili ndi magawo awiri: A ndi B**

3. Lembani **dzina lanu** pamwamba pa tsamba **lililonse loyankhirapo.**

4. Muchitebulo chili pambalichi, onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.

5. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani funso ngati mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| | Total | | |

© 2026 CEED **Turn over**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Gawo A (Malikisi 40)**

**Chimangirizo KAPENA Kalata**

**Malangizo:**

1. Yankhani funso **limodzi** lokha m'gawo ili. Musatenge nthawi yoposa ola limodzi ndi mphindi khumi poyankha funsoli.

2. Lembani chimangirizo **kapena** kalata pa masamba **3** mpaka **6**. Mawu a chimangirizo kapena kalata asachepere **300** koma asapitirire **400**.

3. Malikisi adzaperekedwa pakayalidwe ka chimangirizo kapena kalata, malamulo a chiyankhulo, Mfundo ndi kagwiritsidwe ntchito koyenera ka nsinjiro za chiyankhulo.

1. a. Lembani chimangirizo pa mutu uli m'munsiwu:

Kuipa kosatsatira malamulo a pa sukulu

**(Malikisi 40)**

**KAPENA**

b. Lembani kalata kwa mlangizi wazamalimidwe, yomupempha kuti adzakuphunzitseni ubwino wa ulimi wakasakaniza m'dera lanu.

**(Malikisi 40)**



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

© 2026 CEED



Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

© 2026 CEED



Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

© 2026 CEED



Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Gawo B** (Malikisi 20)

**Za Chikhalidwe**

**Yankhani mafunso onse m'gawo ili.**

**2.** Werengani malonje alembedwa m'munsimu ndipo muyankhe mafunso otsatirawo pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

**"**Moni nonse. Ndaitana ndine kuti tilumane makutu malinga ndi chipalamba chazungulira mudzi wathuwu. Izitu sikuti zangobwera ngati chidzam'mphepo, ndife tazikodola. Ndiye poti chati deru chaopsa mlenje, ndimati tichite machawi pokozanso chilengedwe. Wina asachite mtudzu, apo bii, akugwa apa zabweya zitatu. Kalowam'malaya wakhala akutichotsa chimbenene chifukwa cha ife tomwe. Tayeretsa mitengo posakasaka khobidi lopulululuka ngati mchira wa khoswe.

Tisasandutsenso anzathu akapalemoto pa ntchitoyi. Tikuyenera tiyendere limodzi mwanyerere popeza mu umodzi muli mphamvu. Tikatero, tidzaona kuti gaga m'mudzi mwathu muno adzayangatidwa ndi aliyense pamodzi ndi inu nomwe mukubisala mchirere, misana ikuonekera, ponena kuti nkhongono zotchaira mphanje m'thupi mwanu zidayamba zasamuka."

a. i. Angayankhule mawu amenewa ndani?

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

ii. Kodi ndi vuto lanji lachititsa kuti msonkhanowu auitanitse?

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

iii. Woyankhulayu akufuna kuti anthuwa atani?

_______________________________________________ **(Maliksi 1)**

© 2026 CEED



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

iv. Ndi khalidwe **limodzi** liti lomwe woyankhulayu sakufuna anthu ake achite?

_____________________________________________ **(Malikisi 1)**

b. Perekani matanthauzo a mawu omwe ali m'munsimu monga agwiritsidwira ntchito m'malonjewa.

(1) kalowam'malaya ______________________________ **(Malikisi 2)**

(2) mu umodzi muli mphamvu ________________________ **(Malikisi 2)**

(3) gaga ___________________________________ **(Malikisi 2)**

(4) mukubisala pachipande __________________________ **(Malikisi 2)**

(5) zabweya zitatu ______________________________ **(Malikisi 2)**

c. Ndi malangizo **atatu** ati omwe mungapereke kwa mnzanu yemwe walandira mankhwala achifuwa chachikulu ku chipatala?

1. ______________________________________________________
2. ______________________________________________________
3. ______________________________________________________

**(Malikisi 3)**

d. Perekani njira **zitatu** zomwe mungatsate pofuna kufalitsa uthenga oitanira anthu ku ntchito yokumba chitsime m'mudzi.

1. ___________________________________________ **(Malikisi 1)**
2. ___________________________________________ **(Malikisi 1)**
3. ___________________________________________ **(Malikisi 1)**

# MAFUNSO ATHERA PANO

**NB: Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi atatu.**

© 2026 CEED



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com